

ZAKATI ILI MMAGULU AWIRI

1-YA SUNNAH: Ndipo ichi ndi chuma chilichonse chimene munthu amapeleka mu njira ya ibadah (kumpembedza Mulungu).

2-YA FARADH (YOKAKAMIZIKA)

Iyi ili mmagulu awiri:

ZAKATI YA ZAKUDYA:

Iyi ndi imene imatchedwa kuti Zakatul fitir, imene imapekedwa ku mapeto kwa mwezi wa Ramadhani, ndipo ndiyokakamizika kwa msilamu aliyense, wamkulu, wamng'ono, wammuna kapena wamkazi, kapolo kapena mfulu.

ZAKATI YA CHUMA (NDALAMA):

Tanthauzo lake pa sharia: uku ndi kumpembedza Allah popeleka gawo lomwe lili lokakamizika pa sharia kuchokera mu chuma chodziwika bwino, chumacho chipite ku kagulu kapena mbali yodziwika bwino. Ndipo imeneyi ndi msichi yachitatu mu msichi za chisilamu.

Zakati imeneyi ili mmagulu anayi(4).

1
Golide ndi Siliva kumpatikizaponso mtundu ulionse wa ndalama (ngati ma kwacha). Golide mulingo wake ndi 20 (omwe ndi ma galamuzi 85). Pomwe mulingo wa Siliva ndi 200 (omwe ndi ma galamuzi okwana 595).

NDALAMA ZIWIRI



4

CHUMA CHA MALONDA



Ichi ndi chilichonse chimene chaikidwa pa mndandanda wa kugula ndi kugulitsa (bizinesi).

3

ZOTULUKA MU NTHAKA



Izi ndi Njere (monga chimanga) Ndi Zipatso (monga tende)

2

ZIWETO



Zimene gawo lalikulu pa chaka zimadyetsedya ndi msipu waulele. Ndipo ziweto zake ndi monga: Ngamila, Ng'ombe, Mbuzi kapena Nkhosa.

ENI ZAKATI (OYENERA KULANDILA)

Awa ndi omwe amapezako zowathandiza zochulukilapo kapena theka pa Chaka. Titati tiyelekeze kuti ndalama imene ingakwanire kudya pa chaka ndi K12000. Ovutika aja ndiye kuti akhala ndi K6000, kapena alibiletu. Pomwe osaukawa ndiye kuti akhala ali ndi K6000 kapena kuposela pamenepo, koma safika pa K12000. Choncho ife timayenera kumpatsa ovutika ndi osauka yu chimene chingawakwanire pa chaka. Zili choncho chifukwa zakati imakakamizidwa chaka chikazungulila.

OSAUKA (MISIKINI)

2

Awa ndi ovutika omwe sapeza kalikonse, kapena amapeza zowakwanira zochepa kwambiri pa moyo wawo.

OVUTIKITSITSA (MA FUQARAU)

1

Awa ndi omwe amatolera, kusunga ndi kugawa zakati. Ntchito imeneyi amapatsidwa ndi mtsogoleli. Awa amapasidwa zakati osayang'ana kuti ndi osauka kapena olemela. ngakhale ali olemela amayenerabe kuti apatsidwe zakah.

OGWIRA NTCHITO YA ZAKATI:

3

Awa ndi omwe timayembekezera kuti atha kulowa chisilamu, kapena kusiya kwavutitsa asilamu (ngati atsogoleli adera) kapena omwe tikufuna kuwalimbikitsa chikhulupiliro chawo (imaan).

OFEWETSEDWA MITIMA YAYO

4

Umu mukulowa asilikali a nkondo ndi kalikonse kamene angasaukile monga zida ndi zina zotero.

YEMWE ALI PA NJIRA YA ALLAH

7

Awa ndi: A- Msilamu yemwe walembedwa kuti ngati atapeleka ndalama mwakuti basi amasulidwa ukapolo. B- Kummasula ukapolo msilamu. C- Msilamu yemwe wagwidwa ukapolo ku nkondo.

AKAPOLO

5

Uyu ndi munthu yemwe wauyamba ulendo ndipo kamba wake wa pa ulendo watha (monga tarasipoti), choncho amapasidwa zokamufikisa kwawo komwe wachokera kapena komwe akulowera.

WA PAULENDO

8

Awa ndi: A- Yemwe wagwa mu ngongole chifukwa chofuna kuyanjanitsa anthu omwe asemphana. B- Yemwe wagwa mu ngongole chifukwa chofuna kuzithandiza pa mavuto ake omwe anamugwera.

OTHINIDWA NDI NGONGOLE

6